


# CHOLEMBEDWA PA KHOMA

 Uno pokhala usiku wa lachitatu, paja ndinalonjeza usiku watha ujanso, kuti Ambuye akalola, usiku uno, ndilankhula pa mutu wa: *Cholembedwa Pa Khoma*. Ndi wakuti. . . O, tikhoza kutenga masabata pa mutuwo, ndipo sitingakhoze kukanda pamwamba pokha. Koma ndiyesa kungofotokoza pang’ono pake usiku uno, mwa chithandizo cha Mzimu Woyera. Ndipo tsopano ndifuna kuwerenga kuchokera mu Daniele, mutu wa 5 ndime 25. Ndipo pakuwerengeka chotere.

“Ndipo izi ndi zolembe zimene zinalembedwa, MENE, MENE, TEKEL, UPHARSIN.”

Ndipo tsopano Ambuye awonjezere madalitso Awo pa kuwerengaku.

<sup>2</sup> Ndipo ndikudabwa ngati m’bale wathu wabwino, woyang’anira malo ano, angazimitse magetsi owala kwambiriwa. Ine ndiwo. . . Akundiwalira kwambiri panopa. Zikomo, mwandikomera mtima kwambiri. Sindimawona anthu onse. Kotero pamene ndikulankhula kwa aliyense, ndimafuna ndiziwayang’ana pa nkhope pamene ndikulankhula. Zimakhala ngati ukulankhula ndi aliyense wa anthuwo payekha.

<sup>3</sup> Tsopano tikudalira kwa Ambuye wathu, usiku uno, pamene tikufuna ndingoyesa kutenga nthawi yanga ndi kulankhula pa mutu uwu. Ndikudziwa kuti ndi phunziro lalikulu. Ndipo ndi ulaliki wotembenezira anthu, osati wo-handizira machiritso Auzimu. Koma ndi wa machiritso opambana Auzimu. Thupi lodwala kwambiri limene ndikulidziwa usiku uno, ndi Thupi lauzimu la Ambuye Yesu, pa dziko lapansi lino; lang’ambika, ndipo laphwasuka, mpaka kuti likusowadi machiritso Auzimu.

<sup>4</sup> Tsopano, phunziro lathu usiku uno likuyambira ku Babeloni. Ndipo Babeloni poyamba anali, komwe kuli mpaka lero, ku Shinari. Ndipo poyamba kunali katchedwa “chipata cha Mulungu,” *Babulo*. Babulo, kenaka anatchedwa *Babeloni*, chimene chitanthauza “*chisokonezeko*.” Ndipo Babeloni amapezeka koyamba kwa Baibulo, ku Genesis; ndipo amadzapezekanso pakati pa Baibulo; nadzapezekanso kumapeto kwa Baibulo, mu Bukhu lotsiriza, Chivumbulutso. Ndipo pakuti akupezeka mu Baibulo lonse, kotero ayenera kukhalapo ngakhale lero.

<sup>5</sup> Ndiponso, zonse zimene ziri pa dziko lapansi lero, mwa njira ya zinthu zauzimu, monga za Mzimu wa Mulungu ndi mzimu wa Mdierekezi, ndi miyambo ndi zina zonse zimene tiri nazo lero mu dziko, zinayambira ku Genesis. *Genesis* amatanthauza “Chiyambi.” Ndipo zinthu zonsezo, ngakhale zinali ndi mayina ena ndi maonekedwe ena, koma mzimu womwewo umene

unayambitsa izo ku Genesis, ukuzitulutsanso. Ndipo ziri ngati mtengo umene ukukula, kufika pamutu wake, pamene uti ufike pa chimake pamapeto, kuti ulandire chiweruzo chopambana cha Mulungu, pamene Iye adzakhazikitsa zinthu zonse. Ndipo zonse zimene zinali ndi chiyambi zidzakhala ndi chitsirizo. Kupatula zinthu zokhazo zimene zinalibe chiyambi izo ziribe mapeto.

<sup>6</sup> Chimenecho ndi chifukwa—Akhristu obadwanso kachiwiri alibe mapeto, chifukwa ali ndi Moyo Wamuyaya. Ndipo Moyo Wamuyaya ndi gawo la Moyo wa Mulungu Mwini, pakuti Mulungu ndi Wamuyaya. Ndipo liwu lomwelo, liwu la Chigriki lakuti *Zoe* limatanthauza “Moyo wa Mulungu,” pamene Yesu alankhula nati, “Ndimapereka kwa iwo Moyo Wamuyaya,” liwu lomwelo likugwiritsidwanso ntchito. Kotero, munthu pamene abadwanso, mzimu wake wasinthika, ndipo iye amasandulika gawo la Mulungu, mwakuti iye ndi mwana wa Mulungu. Ndipo iye amangokhala Wamuyaya monga momwe Mulungu ali Wamuyaya, chifukwa iye ndi gawo la Mulungu, mwa Kubadwa kwake, Kubadwa kwauzimu.

<sup>7</sup> Tsopano, Babeloni anayambitsidwa ndi munthu wotchedwa Nimrodi, amene anali mwana wa Hamu, munthu woyipitsitsa.

<sup>8</sup> Ndipo Babeloni poyamba anali likulu la dziko lapansi. Pamene mzinda waukuluwu unamangidwa kumeneko, timizinda tating’ono tina tonse, pozungulira iwo, anali kupereka ndalama, misonkho, ndi zina zotero, kwa mzinda waukuluwu, Babeloni.

<sup>9</sup> Ndipo m’menemo, ngati mutawerenga mu mabuku akale, monga *Two Babylons*’ la Hislopu, ndi mabuku a mbiriyakale mukapeza kuti anali ndi tiziphunzitso tachilendo tambiri m’menemo. Anali ndi mkazi m’menemo, sindingatchule dzina lake nthawi ino, ndipo iye ankakhoza kupeza mitsitsi yamaonekedwe achilendo, mu nthaka, namapanga timilungu kuchokera mwa iyo. Zikukhulupiridwa kuti timeneto tinali timilungu timene Yakobo anawabera atatabzala ake, tina ta timilungu ta mitsitsi imeneyo motero. Monga timachitidwe tokhazikitsidwa, ndipo kuchokera mu zinthu zimenezo machitidwe awa amene tikuwawona mdziko lero. Ngati mutayang’anitsitsa khalidwe la zimenezo, ndi khalidwe la zinthu izi za masiku ano, khalidwe lake ndi lofanana.

<sup>10</sup> Kotero, Babeloni anali mu chigwa chachikulu cha chonde kumeneko, ndipo chinazunguliridwa ndi kuthiridwa ndi Mtsinje wa Efurate ndi Tigrisi. Ndipo linali likulu lotchuka la ulimi. Ndipo Babeloni anali mzinda waukulu. Ndipo unali, pafupifupi, mamailosi 120 kuti uzungulire mzindawo; mamailosi 30 mbali iliyonse, palimodzi kukhala 120 mailosi kuzungulira. Akuti misewu ya mumzinda wa Babeloni inali mapazi 200 kutambalala kwake. Makoma ake anali mapazi 80 kukandapala kwake, ndipo anali mapazi 200 kumene kutalika cha m’mwamba. Amakhoza kuchitira mijaha ya magareta

pamwamba pa makomawo, atakwera magareta. Ndipo zipata zake zinali zopangidwa ndi chitsulo cha mkuwa, ndipo zipata zimenezo kutambalala kwake zikanakhala mapazi 200. Ndipo pakati penipeni pa mzindawo panali nyumba ya mfumu, ndipo ku nyumbayo kunali mpando wachifumu. Ndipo mopyola pakati pa mzindawo kunadutsa mtsinje waukulu, Efurate. Ngati mutawonetsetsa, umenewu ndi mzinda wa Mdierekezi, pakuti unapangidwa mofanizira Mzinda wa Mulungu, pamene Mtsinje wa Mayo uchokera ku Mpando wachifumu. Ndipo mu mzinda umenewu, anali ndi minda yaikulu, ya m'malere, yoyandama m'makoma, mozungulira.

<sup>11</sup> Ndipo unali ufumu waukulu, wamphamvu chotero pa nthawi imeneyo, mpaka kuti unagonjetsa maiko onse amene ankadziwika, ndipo dziko lapansi lonse linali kulipira msonkho. Unatukuka koposa mu sayansi, ndipo unali ndi zinthu zamakono zimene sayansi imakhoza kupanga. Unali ndi magaleta a nkondo amakono, a kapangidwe kamakono, zida zodzitetezera zamphamvu koposa, zopangidwa ndi zitsulo zolimba. Unali mzinda wa pamwamba padziko lonse lapansi.

<sup>12</sup> Ndipono mkati mwa makoma amenewa, komwe Mfumu Belteshazzar anali mfumu pa nthawi ya chochitika ichi chimene tikuchikamba usiku uno. Mfumu Belteshazzar, amene Baibulo limati, “Nebuchadnezzar, amene anali bambo wake,” koma moona anali agogo ake amene iye analowa m'malo mwawo, Mfumu Nebuchadnezzar.

<sup>13</sup> Ndipo ambiri a inu mukukumbukira kuti Nebuchanezzar anali woyamba wa maufumu a Amitundu, mutu wa golide. Ndipo iye anapita mpaka ku Yerusalemu, mwa mailosi ambirimbiri kutali, ndipo anakagwirako Ayuda nadza nawo mpaka ku ufumu wake, nawachititsa iwo kukhala akapolo, ndipo anagwiritsanso ntchito anthu asayansi awo ndi zina zotero.

<sup>14</sup> Monga momwe Russia anachitira pamene anapita ku Jeremani. Ndipo pamenepo ndi momwe anapezera bomba la atomiki, ndi zina zotero, anagwira anthu a sayansi aku Jeremani. Ndi chifukwa chake ali otukuka kwambiri motero lero, anagwira iwo nawatengera kwawo. Iwo wokha, analibe izi, koma anapita nakatenga zinthu zimenezo monga momwe Nebuchadnezzar anachitira ndi Ayuda.

<sup>15</sup> Ndipo tikupeza kuti, kuyambira pa nthawi imeneyi, kunali munthu wolungama dzina lake Danieli, m'neneri wa Ambuye, amene anatengedwanso kupita ku ukapolo pa nthawi imeneyo. Iye anatomikira monga karonga wa onse oyang'ana nyenyezi ndi zina zotero, ndi pa amuna anzeru ndi a Magi, pa nthawi ya ulamuliro wa Mfumu Nebuchadnezzar.

<sup>16</sup> Ndipono Belteshazzar anadalowa ufumuwo. Belteshazzar anali munthu woyipa mtima. Iye sankasamala kanthu!

<sup>17</sup> Ndipono anthu onse a mu Babeloni, ndi chitetezo chimene iwo ankawona ngati anali nacho! Pamene ali mkati mwa zipata zimenezo, ndipo zipatazo zitatsekedwa, ndi makoma awo otalika mapazi 200, onenepa mapazi 80, tangoganizirani momwe iwo amadziwonera ngati otetezedwa mkati mwa makoma amenewo!

<sup>18</sup> Koma ingokumbukirani ichi. Ngakhale sayansi ikutetezeni chotani, Mulungu adzakupezani momwemo ngati muchita tchimo! Pali chitetezo chimodzi chokha, ndipo ndicho mwa Khristu Yesu.

<sup>19</sup> Tsopano, momwe iwo anadziwonera monga opambana kwambiri pokhala fuko lotsogolera mdziko, chimodzimodzi kwenikweni, momwe chitukuko cha makono monga chomwe tikukhalamochi, Amerika wapamwambayu. Ndipo ine ndikusautsika, inemwini, koma ndikuwopa kuti tikutenga khalidwe limene iwonso anatenga. Kuti tikuwona ngati pakuti tiri nazo, zomwe tikuganiza, a sayansi opambana, ndi mfuti za mizinga zopambana ubwino, ndi mabomba atomiki, ndi ndege zothamanga kwambiri, ndipo tangochita ngati. . . Pokhala fuko lotsogolera mdziko, tayamba mwa njira yina kumverera chitetezo chathu popanda Mulungu.

<sup>20</sup> Ndi ndondomeko yokongola kwambiri. Ndipo Mulungu samasintha. Momwe Iye ayang'anira pa tchimo ndi chimodzimodzi lero monga zinaliri nthawi iyo. Ndipo palibe malo obisalapo pansi pano. Mwa Khristu yekha ndinu otetezeka.

<sup>21</sup> Ndipo mu mzinda wotchuka uwu, monga momwe anawonera ngati panalibe njira yina, mdziko, kuti gulu la ankhondo lingadzalande mzinda umenewo. Makoma akulu, atali ndi zida zawo zamakono, ndipo iwo anali otchingiridwa kwa dziko lonse lakunja kwawo. Koma anadziwa pang'ono za fuko loyipa lotchedwa Amedi ndi Aperesi, amene tsopano ndi a Hindu a ku India, kudziwa kwawo kunachepa kuti mamailosi ambiri kutali iwo anali kukumba mphepete mwa mtsinje, kuti apotoze Mtsinje wa Efirate, kuti iwo adzakhoze kuyenda pansi pa makomawo. Pamene iwo anadziwona otetezeka! Nthawi yonse iwo amangodziona motero. Pamene anali kudziganzira motero, ndiyeno anapitirira kusambira m'machimo.

<sup>22</sup> Zimawoneka ngati pamene munthu afika pa malo odziwona ngati iye ndi wodzidalira, tchimo limayamba kumugwira. Mpingo, fuko, munthu pa yekha, amene awona kuti sasowa chithandizo chirichonse chochokera kunja, tchimo limayamba kumulamulira. Izo ndi zowona. Ndipo tikhoza kuwonanso, kuti pamene anthu ayamba kudziwona ngati otsogola, kawirikawiri ndi pamene tchimo limawalowerera niliwavunditsa.

<sup>23</sup> Kotero pamene iwo anatseka makomowo, anaganiza kuti anali otetezeka. Koma Mulungu amayang'ana pansi kuchokera kumwamba! "Ndipo tchimo liri themberero kwa fuko lirilonse."

24 Ndikudabwa, usiku uno, ndi zida zathu zopambanazi, ndi sitima zathu zomira m'madzi zowongoleredwa ndi mphamvu ya atomiki, ndi ndege zathu zowuluka mamailosi mahandirede ambiri pa sekondi, kuti ngakhale...kapena miniti, zimene zikhoza kuthamanga mofulumira kuposa mkokomo wake womwe. Koma, musayiwale konse kuti machimo anu adzakupezani!

25 Ndipo, mu nthawi iyi, iwo anali atatseka zipata. Ndipo iwo anaganiza kuti akhoza, angathe kumangoyimba akuvina momwe angafunire, chifukwa anali otetezeka. Iwo anali fuko lotsogola, mafuko ena onse ankayang'ana kwa iwo pa za sayansi ndi pofuna—pofuna chithandizo.

26 Koterono, panthawi yotereyo, panali a...Mfumu iyi inaganiza kuti ikhoza kudzipatsa nthawi yabwino yopambana. Ndipo iye anakonza tsiku limene anafuna kuti kudzakhale kuvina kopambana kwakukulu, kapena, momwe ndikhoza kunena kuti, zofanana ndi gwedemula wa makono; palibenso zoposa zimenezo. Koterono iye anakhazikitsa nthawi, ndipo anayitana onse otchuka, asirikali onse ndi akapitawo, ndi akazi awo onse ndi akazi awo apadera omwe.

27 Tsopano, akazi awo apadera ndiwo mahule oloedwa ndi boma. Ndipo nanga mukuwonano, pamene munthu ayamba kudziwona ngati wodzidalira, kuti amayamba kusambira m'machimo?

28 Ndipo anayitanitsa mowa wapamwamba umene akanaupeza, wa pa phwando la gwedemula limene anali kudzakhala naloli. Iye anaganiza kuti anali wotetezeka. Iye anaganiza kuti panalibe chimene chikanamupweteka, chifukwa anali wotetezeka. Ndipo iye anachita phwando lopambanali pa bwalo la kuseri kwa nyumba yake yaufumu. Ndipo pamene anali kubwalo lomwelo, mwina anali atalikongoletsa kwenikweni, pali ziyangoyango ponsepo, ndipo anatenga akazi ena onse a sankhawekha ndi azimayi ambiri kuti abwere kudzasangalatsa asirikali. Ndipo mowa wawo ndi vinyo wawo! Ngati izo sizikugwirizana ndi momwe amachitira makono ano pa phwando la gwedemula lero, sindikudziwa mwina momwe zingakhalire. Ndi chimodzimodzi. Ndipo zonse zinali zitakonzeka, ndipo anakonzekeradi kudzakhala ndi nthawi yaikulu.

29 Ndipo mosakayika ngakhale akazi okwatiwa ambiri omwe anadza. Amuna awo anawasiya kunyumba akulera wana, pamene iwo anapita kukakhala ndi nthawi yabwino. Ndiponso mbali yinayinso, mosakayika amayi anali akungozungulira, ndi mwana wodwala, pamene amuna awo oledzera anapita kukakhala ndi nthawi yaikulu. Zinali theka la ena, ndi theka lina enawonso.

<sup>30</sup> Ndipo ndikhoza kuwawona pamene anayamba kumwa ndi kukhala ndi nthawi yayikulu. Ndipo ndikhoza kuganiza kuti gulu loyimba linalindimuka, ndipo linaziyamba nyimbo. Ndipo ongopitirira zaka khumi anayamba kuzunguzana. Ndipo asirikali, ataledzera, kumagwira akazi ndi kumawaponyera pamitu yawo, ndi kumawapsyonapsyona nawakhazika pamipando, onse nayamikira. Kumaganiza kuti anali otetezeka!

<sup>31</sup> O, Amereka, Mulungu amene anayang'ana pansi pa anthu awo ataledzera, phwando la gwedemula, akuyang'ana pa iwe usiku uno!

<sup>32</sup> Ndipo inali nthawi yopambana motani imene anali nayo! Ndipo ndikhoza kulingalira kuti mfumu iyi apa, Belteshazzar, anali monga Elvis Presley wamakono, ankakhoza kuchita zambiri za zosangalatsa zawo zimene anali nazo. Ndipo zochitachita zawo zonse, nasamadziwa, nthawi yonse, kuti imfa inali pakhomo!

<sup>33</sup> Kotero, pamene phwando linagundika, kawirikawiri zofanana ndi zopambana zimene zikuchitika makono ku chiwonetsero cha Hollywood, iwo anaganiza kuti akanakhoza kuswa nthabwala zina zabwino zokhudza chipembedzo, monga zonena za Arthur Godfrey, kapena zina zotero zamakono lero, kapena za Ernie Ford mtola-nyemba, kuswa nthabwala zokhudza alaliki. Koma Mulungu akuyang'anabe pansi kuchokera Kumwamba! Koma iwo anali kuganiza kuti amakhala mufuko limene linali lakuti nkuchita nalo masewera. Koma umakolola zimene wabzala!

<sup>34</sup> Ingochenjerani nazo zimenezo, anthunu. Kaya ndinu fuko, kapena mpingo, kapena munthu pa yekha, mumakolola zimene mwabzala!

<sup>35</sup> Ndipo, bwanji, ndikuwona mfumu iyi ikuyimirira, niti, "Tayembekezani pang'ono, atsikana, tiyeni tikhale ndi nthabwala ya chipembedzo yokhudza alaliki," ndi zina zotero.

<sup>36</sup> Ndipo tinsalu tonyezimira tinakupizidwa, ndipo asungwana anati "Eeyaa! Inde, ife tikukhulupirira kuti tikonda kumva imeneyo."

<sup>37</sup> Ndipo asirikali achinyamata anapokosera monga momwe amachitira anyamata ongopitirira zaka khumi lero, pakuti izi sizikusiyana ndi za Babeloni wamakono! Ine ndi wa Chimerika, komanso Daniele anali wa mu Babeloni pa nthawi imeneyo. Koma zimenezo sizingapetsere tchimo!

Ndinati kwa msungwana nthawi yina, "Kodi ndiwe M'khristu?"

Iye anati, "Ndikupatseni kumvetsa kuti, ine ndine wa Chimerika."

Ndinati, "Zimenezo sizitanthauza kanthu." Ndi pang'onoponse ayi!

38 Ndine wosangalala pokhala wa Chimerika, koma zimenezo ziribe kanthu kowonetsera Chikhristu; sikanthu konse. Ngati ife tichimwa, tidzalipira chifukwa cha machimo athu, ichi chikhale chotsimikizika kwa inu.

39 Iwo anali ndi m'neneri kumeneko, koma iwo sangamvere. Iwo anali nawo Uthenga, koma ankangofuna kumanenera zoselewula pa Iwo.

40 Ngati izo sizofanana ndi Amerika wamakono, sindikudziwa. Iwo anali ndi Uthenga, Choonadi, koma amangokonda kuwuselewula Iwo.

41 Kotero anati, "Tiyeni tipite tikatenge ziwiya za anthu odziyeretsa aja, ndipo tidze nazo kuno ndikudzachita nazo nthabwala zabwino."

42 Mulungu salola ochimwa kuti aziseka anthu Ake! Mudzalipira pa zimenezo, tsiku lina.

43 Ndipo anapita nakatenga ziwiya za Ambuye, nadza nazo kuzichotsa mu kachisi, ndipo anafuna kuti amwere bwino mu ziwiya za Ambuye. Ndipo pamene anathira mowa wa Oertel's 92 kapena Pabst Blue Ribbon, m'menemo, kuti achite nthabwala yabwino nazo, o, iwo anagunditsa magalasi awo ndi zikho, nayamba kumwa, namaseka ndi kunyodogola chipembedzo cha Ambuye. Iwo sanali kudziwa zimene anali kuchita.

44 Ndi momwe lirinso fuko ili, usiku uno, sakuzindikira kuti akana Uthenga wa Ambuye Yesu Khristu, mu ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi kubadwa kachiwiri.

45 Ngakhale anali a chipembedzo, tsopano, phwando limenelo loledzererapo ndi kuvina gwedemula, iwo anali anthu azipembedzo, pakuti Baibulo linatero kuti, "Iwo anali kutamanda milungu yawo."

46 Kotero ukhoza kukhala wachipembedzo nthawi zonse chotero, nukhalabe wolakwa! Nzoonadi. Sikudziperekako ayi. "Pali njira imene imawoneka ngati yolondola kwa munthu, koma mapeto ake ndi njira ya imfa." Kotero iwo anali ndi mpingo waukulu wa boma, ndi chipembedzo chimene amakhoza kutumikira, ndipo ananyodogola zinthu zopatulika za Mulungu.

47 Ndipo zimenezo ziri chimodzimodzi ndi za lero, kumangonyodogola zinthu zopatulika za Mulungu. Iwo amawatcha anthu, amene akuyesa kukhala moyo woyera ndi wabwino, ndi wolunjika, amawatcha iwo, "achikale" kapena "odziyeretsa," kapena mtundu wina wa mayina onse onyoza. Ndipo amatcha mpatso za Ambuye, zimene Iye akuwonetsera, "Ntchito za mizimu yoipa, monga wam'bwebwe kapena mdierekezi." O, mungathawe bwanji chiweruzo? Magazi a anthu oyera mtima akufuula motsutsana nazo zimenezo! Ngati Mulungu sangaweruze fuko ili chifukwa cha tchimo lake la makono, Iye adzayenera kudzutsa Sodomu ndi Gomorah,

nawapepesa chifukwa chowawononga iwo. Ndi zoon. Ife talunjika ku chiweruzo! Ndipo zodabwitsa zopambana zimene mukuziwona Mpulumutsi wathu wodala akuzichita, izo ndi zizindikiro zotichenjeza, kuti chiweruzo chiri pafupi; ndipo chawonetsedwa kwa fuko lonseli mbali ndi mbali, kuchokera Kum'mawa mpaka Kumadzulo, kuchokera Kumpoto mpaka Kum'mwela. Ndipo iwo akungochikankha Icho, nachiseka Icho, kuchitsutsa Icho, nachilemba mu mapepala awo nati "ndi za nkutu." Tangoganizirani izi, Babeloni wamakono!

<sup>48</sup> Tsopano pamene iwo anali kumwa, kugundanitsa zikho zawo pakumwa; mwadzidzidzi, pamene mnyamata wopambana wasewero wawoyu, wotchedwa Belteshazzar, anali wokonzeka pafupi kuti amwere mu chikho chake, maso ake anangowoneka ngati atong'oka, pamene anatembenukira mbali ya ku nyumba yachifumu, pakuti anawona, kuchokera Kumwamba, dzanja la Munthu, ndipo linayamba kulemba lemba pa khoma.

<sup>49</sup> Ndikufuna inu kuti muwonetsetse, Ilo linalimba pa pulasitala. Tsopano, kapena zoyikapo makandulo zinali pa choyandamitsira pake, kumene iwo anali ndi gule wawo wagwedemula wamakonoyu, ndipo kuwala kwake kwamawonekera pa khomalo. Mulungu samachitira zinthu pakona! Ndi powala kwambiri pomwepa, pamene Mulungu amalankhula nayendayenda. Koterokulemba Kwake kwauzimu kunali pa pulasitala ya pa khoma, pamaso pa iwo onse.

<sup>50</sup> Ndipo mfumu ayenera kuti anali amene anachiwona ichi poyamba, wanthabwala wamakonoyu, namatetule wa pa walesi, wosangalatsa pa televizioni. Pamene ankati apendeketse galasi lake, kuti amwe, kapena titi chikho, chimene iye anali nacho m'manja ake, maso ake anatong'oka, ndipo ananjenjemera kwathunthu. Ndikungolingalira kuti anatero. Baibulo limatero kuti, "Mafupa ake anagweruka, mu mfundo zake." Moonadi iye anali njenjenje, kotheratu ndithu. Pamene Mulungu ayamba kuwonetsa zizindikiro Zake, ndi nthawi yonjenjemeretsa. Ndi zoon. Ndipo pamene iye anawona ichi, nyimbo yake ya gwedemula yomwe imamunjenjemeretsa.

<sup>51</sup> Ndipo pamene iye anawona zolembedwa pakhomapo, ndikhoza kungoganizira kuti kamkazi kake kotumikira kali milomo pake pake ngati sindikudziwa-chiyani, ndipo tsitsi lake atayikamo zonyezimiritsa, kakungodukaduka poyenda, ndi asirikali oledzerawo pamenepo, kanati, "Ndikudabwa chimene chachitika ndi njondayi usiku. uno?" m'menemo kakupanga ntchirikiro.

<sup>52</sup> Ndipo m'nyamata wina anamugwira iye, nati, "Ziribe kanthu, tiye tivine nyimbo inayo limodzi." Ndipo kuyimba kunalekeka.

<sup>53</sup> O, fuko lopambana kuchuluka machimo ili, nthawi yina gwedemula wanu adzaleka! Ngati simumvera liwu la wolalikira,



mudzamvera dzanja la Mulungu mu chiweruzo tsiku lina. Koma gwedemula adzaleka, chimodzimodzi momwe oyimba anachitira, nayamba kuyimba “*Mfupi, Mulungu Wanga, ndi Inu*” pa Titanic ija. Tsiku lina mudzasintha kayimbidwe kameneko.

<sup>54</sup> Ndipo nyimbo zinalekezedwa. Ndipo iwo anawona kuti wanhabwala wawo-kaswiri wawo wa pa televizioni, kuti iye anangoyima, mawondo ake akungowombana, pamene anayang’ana napenya chinthu chopambanachi chikuchitika. “Motani,” iye anati, “makoma athu onse ndi otsekedwa konsekonse. Ndiri ndi alonda anga amene ayima pa chipata, anthu a kusankha kwanga.”

<sup>55</sup> Koma, mukuona, Mulungu samasowa kuchita kudzera pachipata, mwa njira imene inu mukuganizira. Iye anangodza kuchokera ku Ulemerero! Ndipo dzanja Lake linali kulemba pa khomapo.

<sup>56</sup> Ndipo mofulumira, pokhala anali malo a makono kwambiri, Baibulo limati iye anayitana onse a m’bwebwe, ayang’ana nyenyezi, mabishopu onse, ma dokotala, ndi ma papa, ndi ma kadinalo, ndi ena otero. Ndipo anati, “Tsopano ndikuwuzani inu, mabwana, ine ndakupatsani inu mwayi wakumalalika ndi kumachita zimene mukufuna kuchita. Tsopano masulirani, kwa ine, Icho chiri pakhomacho.”

<sup>57</sup> Koma monga momwe zinaliri pamenepo, ziri chonchonso tsopano, iwo sanali ozolowera zauzimu. Iwo sanadziwe kanthu za Ichi. Sanadziwe kumasulira kwake kwa malirime osadziwika. Sanadziwe kanthu za chinenero cha Kumwamba. Ndipo iwo anangokhala akakasi. Palibe chimene anadziwa za Ichi. Ndipo pomwe iwo anali atayima pamenepo. . .

<sup>58</sup> Kumbukirani uku kunali kuyamba kwa ufumu wa Amitundu. Ndipo monga momwe unadzera mwauzimu, udzathanso ndi zauzimu.

<sup>59</sup> Koma mabishopu ndi makadinalo awa, ndi madokotala otchuka, sakanatha kumasulira zauzimu. Palibe chimene anadziwa za Icho. Iwo anayang’ana m’mabukhu awo a luntha, ndipo sanapeze kalikonse kofanana ndi Zimenezo. Mwaona, zinthu zauzimu zimamvetsedwa mwauzimu. Ndipono iwo anali ozunguzika, ndipo sanali kudziwa choti angachite.

<sup>60</sup> Ndipo, potsiriza, kamfumukazi. Kumbukirani, iyeyu sanali pa phwando la gwedemula. Ndipo njira yokha imene iye anali kudziwira kuti chinachake chikuchitika, uthenga unadza kwa iye kuti mfumu ikungonjenjemera, ndipo phwando laleketsedwa. Mkazi uyu akanakhoza kupanga m’modzi wa okhulupira abwino. Ndipo, mwa njira ina kapena imzake, iye anali amene sanayiwali.

<sup>61</sup> Iye anathamangira ku phwandolo. Ndipo pamene anawona wanhabwala wamakonoyo akunjenjemera, ndi gulu lake lonse loyimba, iye anati, “O, mfumu, khalani ndi moyo

wautali!” Koma iye samadziwa kuti anali wakufa pomwepo. Anati, “Khalani ndi moyo wautali! Ine ndikudziwa kuti inu mukusautsika chifukwa cha zolembedwa pakhomapo. Ndipo ndikuwona a papa, ndi mabishopu, ndi makadinalo, ndi madokotala a zauzimu, ndipo palibe m’modzi wa iwo amene angawerenge Icho. Koma, o, mfumu, ndiloreni ine ndikuwuzeni china chake! Pali mwamuna mu ufumu wanuwu, amene amadziwa zauzimu.”

<sup>62</sup> O, m’bale, pamene tikuona zolembedwa pakhoma, lero, koma pali Mwamuna amene akudziwa za zimenezo. Mukhoza kukhala kuti munapita ku maofesi a madokotala onse mumzinda, ndipo anakuwuzani kuti, “Mufa ndithu.” Koma pali Mwamuna! Mukhoza kukhala kuti mwasambira m’machimo mpaka kuti moyo wanu ndi wakuda monga makoma onyansa a Gehena, ndipo mutatsala pang’ono kungodziza, opanda chiyembekezo. Koma pali Mwamuna, ndipo Dzina Lake ndi Yesu! Iye amadziwa zauzimu. Ndipo Iye ali mu Ufumu wathu, pakuti ife tiri ana a Ufumu Wake. Pali Mwamuna!

<sup>63</sup> Anati, “Iye amadziwa zauzimu, pakuti zaka zapitazo anapeza Mzimu wa Mulungu mwa iye. Ndipo iye anali ndi Mzimu wopambana. Iye amakhoza kumasulira maloto, amawona masomphenya, ndi zonsezo zinali zolondola mwa ndendende. Kotero, musakhale ovutika, ingondipatsani ine maminiti pang’ono ndipo ndikabwera naye.”

<sup>64</sup> Padzakhala tsiku lina limene inu mudzamuyitana Iye! Mukhoza kukhala kuti mulibe malo a Iye m’nyumba yanu. Ndinu wotanganidwa kwambiri, kuwonerera televizioni, kusewera juga, kumwa mowa, kukawonerera magule a gwedemula. Koma pali nthawi imodzi imene mudzayitanira pa Iye! Zoonadi.

<sup>65</sup> Ndipo kotero Daniele anabweretsedwa. Ndipo pamene anadza naye. . . Mlaliki wa chilungamo, munthu wa Mulungu! Ine sindikanalingalira kuti munthu wa Mulungu angakhale ku malo oterowo pokhapo atayitanidwa chomukakamiza. Koma, mukuwona, mfumuyu sanasamale kwa Icho, ndi chifukwa chake anapezeka mu khalidwe lomwe iye analimoli.

<sup>66</sup> Ndipo anadza naye Daniele, ndipo iye anati, “Ma papa ndi madokotala anu anakumasulirani inu kuti zimenezi ndi chiyani?” Iwo analibe chakuti angamasulire nacho.

<sup>67</sup> Koterono chinachitika ndi chiyani? Daniele anati, “O, Belteshazzar, inu mukudziwa kale zinthu zimenezi. Sizobisika kwa inu.”

<sup>68</sup> Ndipo ine ndikuti kwa Amerika! Ndikungofuna ndikanawachititsa, pa miniti iyi, kuti amvere mawu anga. Inu simuli osadziwa za zinthu zonse izi! Monga momwe mafuko poyamba anachimwira nachita zimene ife tachitanso, ife tayezedwa mu mulingo, ndipo tapezeka operewera. Chinachitika ndi chiyani kwa Fransi? Chinachitika ndi chiyani kwa

Jeremane? Chinachitika ndichiyani kwa mafuko ena onse amene analowerera ndi “vinyo, akazi ndi nthawi yaikulu?” Zimathera motero nthawi zonse, ndipo ife sitiri otetezeka ku chiweruzo. Mulungu ndi wolungama.

<sup>69</sup> Ndipo iye anati, “Atate wanu, Mulungu anamupangitsa iye kuti akhale ndi fuko lotchuka, koma iye anayiwala zimenezo. Ndipo iye anachita zinthu zofanana ndi zomwe mwachitazi, ndipo Mulungu anamusandutsa iye kukhala chinyama cha mthengo.” Nati, “Inu mukudziwa za zinthu zimenezi, ndipo inu mukutenga ziwiya Zake zopatulika ndi kumazinyodogola.” Taonani. Iye anati, “Zolembe zalembedwa pakhoma, ndipo nthawi ino ufumu wanu wafika pamapedo.” Mwa mawu ena, “Ona apa, munthuwe, masiku ako akwanira! Ufumu wako walandidwa kwa iwe nuperekedwa kwa fuko lina, lankhaza, fuko lopanda umulungu,” limene liri—liri loyipa monga momwe aliri. Mulungu amapangitsa tchimo kumenyana ndi tchimo. Ine ndikudabwa, lero!

<sup>70</sup> Pa nthawi yomweyo, ndineneko poyamba, pamene iye anali chiyimire pamenepo, namayang’ana Zolembedwa pa khoma, sanadziwe kuti pansu pa zipata, nthawi yomweyo, alonda anali ataphedwa. Ndipo asirikali anali m’misewu, kupha alonda anyumba ya boma. Anali pa masitepe. Ndipo akazi awa nkumakhala ataima pamenepo, atasiya ana awo, atasiya amuna awo, amunanso atasiya akazi awo, onse atalezera, akumvetsera magule amakono namachita zawo zawo. Ndipo asirikali anali pa masitepe, mwa maminiti ochepa mutu wa mfumu udulidwa. Chigulu cha amuna oledzera onse chidulidwa mitu, ndi fuko losapembedza, fuko lolamuliridwa ndi m’dierekezi. Ndipo akazi avulidwa zovala zawo, atsikana aang’ono ndi ena onse azichitidwa zoyipa mu msewu; nawanyamula pogwira zitendene zawo, ndi kuphulitsira mitu yawo pamakoma. Kuwang’amba ndi mipeni atatha kukhala nawo mwa kukhumbira kwawo; amisala, asirikali oledzera! Zinali pakhomo, pakuti anali atayesedwa mu muyezo napezeka operewera.

<sup>71</sup> Ndipo ndikudabwa, lero, mwa zochita chita zathu zonse zamakono, kuseka konse ndi kunyogodola misonkhano ya machiritso, kumaseka ndi kumanyoza Mpingo wa Mulungu wamoyo, ndi kumapitirira monga momwe Baibulo linati iwo adzachitira, “Agonthi, odzikweza, okhala nawo mawonekedwe a chipembedzo, koma kukana Mphamvu yake.”

<sup>72</sup> Ndikudabwa, mu tsiku ili pamene tikuganiza kuti tiri otetezeka, ndipo, mwadzidzidzi, titangopezeka kuti Russia ali zaka zisanu patsogolo pathu, mu sayansi.

<sup>73</sup> Takhala tiri ku maphwando ambiri. Tasambira Kwambiri m’machimo. Mpingo wagona kwambiri, siwukusamalanso za misonkhano ya mapemphero. Sizikuwakhuzanso. Akumalankhula motsutsana ndi Mzimu woona weniweni wa

Mulungu wamoyo; iwo sangayanjane nawo. Ali a chipembedzo chotero, ongodziveka! Alibe nthawi ya misonkhano ya mapemphero, amakhala ali pa matelevizioni ndi ku makanema, yaviyavi, ndi ku maphwando oledzera ndi zinthu zina. Izo ndi zowona!

<sup>74</sup> Zimenezo zikhoza kumveka ngati zachikale; koma ndi zimene dziko likusowa lero. Kwachuluka kuseweretsa Uthenga mwachikazi, ndi manja ovala magolofesi. Uyenera kugwiridwa ndi manja enieni mwa mphamvu ya Mzimu Woyera. Zoonadi!

<sup>75</sup> Billy Graham anati, sabata imodzi kapena ziwiri zapitazo, mu uthenga wake wina anati “Dziko lino likhoza kukhala malo oyeserapo zida za Russia, nthawi ina iliyonse imene Russia angafune.” Tiri pati nanga?

<sup>76</sup> Inu mukukhoza kugula marekodi a Elvis Presley, ndi kumakhala kunyumba osapita ku tchalitchi kuti mumvere “*Timukonda Susi,*” yembekezani tsiku lina! Inu mwayezedwa pa muyezo, ndipo mwapezeka operewera! Chachitika ndi chiyani? Pali cholembedwa pa khoma!

<sup>77</sup> Arasha ayika chida cha sputnik m’mwamba chimene ife sitingachilamulire kanthu pa icho, 500 mailosi kuchokera pansi pano; ndipo akhoza kuyika theka la dazeni la zimenezo pamwamba pa Amerika pa maminiti 30 akudzawa, natichitira telefoni nati, “Dziperekeni, kapena mukhale chimulu cha phulusa pa maminiti ochepa.” Iwo akhoza kuchita zimenezo. Palibe chimene ife tingachite kuti tiwaletse. Ziri m’manja mwawo, anthu opanda magazi, opanda mtima, makomyunisiti osawopa Mulungu! Oterowo ndi amene Mulungu amagwiritsa ntchito kuti ayalutse tchimo. Ndithuditu. Ngati mutawerenga Baibulo, Rasha ayenera kuchita zimenezo malingana ndi Chivumbulutso. Chabwino, inu aphunzitsi a uneneri mukhoza kusagwirizana nane pa Zimenezo, koma ingodikirani mpaka zitachitika. Rasha wayikidwa apa ndi cholinga chimenechi. Baibulo limatero.

<sup>78</sup> Tsopano ndi uyu ali ndi sputnik. Ife tinayesa kuti titumize chathu usiku wina, timaganiza kuti tikhoza kuchita mofanana ndi momwe iwo anachitira; chinangonyamuka mapazi atatu okha kuchokera pa nthaka, ndipo chinaphulika. Kuchurukitsa gwedemula ndi tchimo! Ife tayedwa pa muyezo, ndipo tapezeka tiri operewera. Mulungu, khalani wachifundo!

<sup>79</sup> Ndi chiyani chomwe ife titi tichite? Chingachitike ndi chiyani ngati iwo atatumiza ma Sputnik amenewo mmwamba palimodzi ndi ma misayelo amenewo, nati “Dziperekeni, kapena musanduke mulu wa phulusa pa maminiti asanu akudzawa?” Indedi, boma lathu, kuti lipulumutse miyoyo, akhoza kudzipereka. Ndi chinthu chokhacho chimene iwo angachite.

80 Ndiye chingachitike ndi chiyani kwa Amereka enanu, tonsefe pano; osati pano, koma ndikunena fuko lonse? Kunena mwafuko!

81 Inu tiwanthu todzikweza, asungwana amene mumathamanga ndi milomo yanu ya pakepake ngati mitundu yina ya maluwa; ndi kumaseka wolalikira pakona, akulalikira Uthenga. Ndipo inu, tiwanthu tongopitirira zaka khumi, amene mukuganiza kuti muli ndi ubongo wochulukira koposa momwe mungakhalire ndi nzeru za kudziletsa!

82 Chidzachitika chiyani kwa inu, agogo aamuna, amene mumakhala kunyumba usiku ndi agogo aakazi kumawonera televizioni, pamene mwana wanu wa mwamuna ali ku masewera a uzigawenga, ndi mwana wanu wamkazi ali ku kantini kwina kwake, ndipo iye ali kumeneko akuvina gwedemula wake? Ndipo inu mukuwonera televizioni, ndi kumanyodogola Uthenga!

83 Chidzachitika chiyani kwa inu, amembala a tchalitchi? Zotsatira zanu zidzakhala zotani? Mukhoza kukhala nalo dzina lanu mu bukhu lililonse, kapena tchalitchi chachikulu mu mzinda; koma pokha ngati simuli pansu pa chitetezo cha Mwazi wa Ambuye Yesu, mudzawonongeka palimodzi ndi iwo amene adzawonongeka, palibe chiyembekezo kwa inu.

84 Chidzachitika ndi chiyani? Kuli Sputnik m'mwambamo. Ndipo chidzachitika ndi chiyani? Fuku lidzakhoza kudzipereka mogonja, ndithudi, ndi chokhacho chanzeru chimene boma lingachite.

85 Kenako chingachitike ndi chiyani? Mafunde ndi mafunde, a sitima zodzaza ndi asirikali; mafunde ndi mafunde, a ndege; zikhoza kumadzatera mu dziko ili. Akazi akhoza kumangodzachitidwa zoyipa m'misewu. Inu mungamadzatani? Eni ake ndi iwowo. Kutulutsidwa m'nyumba zanu, iwo namadzakhalamo.

86 Chidzachitika ndi chiyani kwa asungwana inu aang'ono, ndi inu anyamata aang'ono, ndi inu nonse pa nthawi imeneyo? Tchimo liyenera kulipiriridwa! Ngakhale litakhala fuko liti, kaya ndi ndani, zikatero zavuta. Aliyense payekha, kapena fuko, liyenera kudzalipira! Ndipo gulu la ankhaza, osawopa Mulungu, anamandevu, asirikali achikomyuminisiti akhoza kumadzagwira akazi anu ndi kuwachita zoyipa, ana anu akazi. Ndipo inu mukhoza kumangodzayima ndi kumazikonda zimenezo, palibe chimene mungachitepo.

87 Chochititsa zimenezo ndi chiyani? Chifukwa mwamvera ku zinthu zosayenera za pa mapologalamu a gwedemula pa televizioni ndi tchimo, ndi ena mwa alaliki ofunda amene sangathe kutanthauzira zinthu zauzimu. Cholembedwa chiri pa khoma! Zimenezo ndi zoon. Ndipo ife tayezedwa pa muyezo, ndi kupezeka operewera.

88 Zimenezo zingadzachitike liti? Dzuwa lisanaturuke m'mawa. Ndani amene angazilete? Yesani kutero. Baibulo limati zidzachitika.

89 Koma ndiroleni ndikuwuzeni, kuti zimenezo sizidzakhudza Mpingo wa Mulungu wamoyo, ife tidzakhala titapita pa nthawi imeneyo!

90 Koteru, mzanga, tamvera. Ngati chinthu ichi chiri pafupi chotero, ndipo ife tikuona cholembedwa pa khoma, palibe chimene chingaletse chinthu ichi kuti chichitike tsopano.

91 Amereka walalikiridwa, zauzimu zachitika, ndipo mopitiriza iwo akungoyandama pamwamba pa izo.

92 Kupita ku dziko lina kukachititsa chitsitsimutso, ndi kukhala ndi otembenuka makumi asanu pa sabata limodzi; ndi kubwererakonso patatha masabata asanu ndi limodzi, ukapeza kulibe ngakhale anayi okha. Dziwe lonse litawezedwa motsiriza. Mulungu ali ndi anthu angapo okha amene Iye anawasankha. Ndipo pamene wotsiriza alowa, ameneyo atseketsa khomo ndipo zithera pamenepo.

93 Ndiye kulibenso china chotsalira koma chiweruzo pamene chisomo chakankhidwa. Ndipo apa tiri pa mapeto a msewu. Zauzimu zikuchitika, anthu akuziseka ndi kuzinyoza. Ndipo chinthu chotsiriza, Mulungu wabwera mwa Mphamvu Yake Yomwe, mwa Mwana Wake Wokondedwa Yemwe, kudzagwira ntchito kupyolera mu Mpingo Wake, ndipo iwo akuti ndi “zaziwanda” kapena “Mdierekezi.” Ndi chiyandinso chimene chingatsalire koposa chiweruzo? Ndipo nachi cholembedwa pa khoma!

94 Koma, ngati ziri zoyandikira chotero, ndipo mphunzitsi aliyense akudziwa kuti Mpingo ukupita mu Mkwatulo chisautso chisanakhazikike. Koteru ngati ziri zoyandikira chotero, zikhoza kuchitika m'mawa usanadze, nanga bwanji Mkwatulo? Uli pafupi kuposa izo! lidalitsike Dzina la Ambuye! Kudza kwa Ambuye kuli pafupi. Cholembedwa chalembedwa, ndipo chinalembedwa mu Baibulo, ndipo ife tikukhala moyo kumachiwona icho.

95 Kodi inu, mwa kukakamiza kwa liwu langa, mungalandire Yesu Khristu ora lino? “Lapani, ndi kubatizidwa,” anatero Petro, “aliyense wa inu, mu Dzina la Yesu Khristu, kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera; pakuti lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa onse amene ali kutali. Pakuti palibe dzina lina limene lapatsidwa pansu pa Kumwamba pakati pa anthu, limene muyenera kupulumutsidwa nalo.” Pokha ngati muli a Khristu! Mukhoza kukhala a Methodisti, Baptisti, Chipentekeste, Nazarene, Katolika, ndinu otayika mpakana pamene mudzakhale a Khristu! Ndipo Khristu nadza mwa inu,

ndiko Kubadwa kwatsopano mwa Mzimu Woyera. Mulandireni Iye usiku uno, pamene tikupemphera.

<sup>96</sup> Ndi mitu yanu yowelamitsa. Ndikudabwa kuti, ndi angati pano amene akudziwa kuti chinthu chachikuluchi chikhoza kuchitika? Mukhoza kupita kukagona usiku uno ndi akazi anu, ndipo m'mawa kupeza iwo atapita. Inu, bambo ndi mayi, mukhoza kuwapsyopsyona ana anu aang'ono pogona, usiku uno, ndipo mawa m'mawa kudzapeza pa kabedi palibe. Ndipo mudzathamangira ku msewu, kuti mukawone zimene zachitika kwa Akazi a Yonasi, nawonso atapita. Mkwatulo uli pafupi, Baibulo lapereka izi momveka.

<sup>97</sup> Ndipo mu msonkhano uwu, pamene muli ndi mwayi, monga ngati mwamuna wa—wanzeru, ndi mkazi wanzeru, chifukwa'nji simukumva kuyitanako mu mtima wanu, ndi kuti, “Ambuye Mulungu, ndidzazeni ndi Moyo Wosatha.” Chifukwa ngati mzimu wanu udakali mwa kumvetisa kwa nzeru, ndinu adziko. Koma Mzimu wa Mulungu, umene umachokera Kumwamba, umadza mu mtima wako nukupatsa Mzimu Woyera, mwa iwe. Pamene chitsautso chidza, Mzimu (Mzimu Woyera) ubwerera kwa Mpangi Wake, ndipo iwe upita palimodzi ndi Iwo. Ngakhale mukhale a chipembedzo chotani, sizingakuthandizeni pokha ngati muli Chinachake mkati mwanu chokutangani.

<sup>98</sup> Ndi angati usiku uno, mutaweramitsa mitu yanu, pamaso pa Uthenga uwu, amene mungakweze manja anu kwa Khristu, nimuti, “Mulungu, ndidzazeni ine ndi Mzimu Wanu Woyera. Ndipo ngati Inu mubwera, ndikufuna kupita ndi Inu?” Kodi mungathe kukweza manja anu? Mulungu akudalitseni, mu tchalitchi monse muno. Kwenikweni, manja 200 kapena ochulukirapo, akwezedwa m'mwamba.

<sup>99</sup> Mzanga wochimwa, ngati simunamulandire Khristu, kodi pa nthawi ino mungakweze dzanja lanu, ndi kuti, “Ambuye Yesu, ndichitireni chifundo ine?” Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu cha kuno, inu kumbuyoko. Winawake, “Ingondikumbukirani ine, Ambuye.” Mulungu akudalitseni inu cha kuno, pamusipa. Ambuye akhale nanu. “Ndikumbukireni ine, O Ambuye. Maso anga atseguka kumene. Ndazindikira kuti mwina ndimangodzinenera kuti ndine M'khristu pa nthawi yaitali, koma sindimadziwa kuti kubadwanso mwatsopano ndi chiyani. Ine ndinali ndisanalandire Mzimu Woyera.”

<sup>100</sup> “Kotero, ngati munthu sabadwanso kachiwiri, sangathe konse kulowa mu Ufumu, kapena kuti sangathe kuwona Ufumu.”

<sup>101</sup> Kodi mungakweze manja anu, ndi kuti, “Ndichitireni chifundo ine, Inu Mzimu Woyera. Ndipo pamene mudzabwera kudzatenga Mpingo, mudzanditenge inenso?” Mulungu akudalitseni inu, dona. Mwina winanso, “Ndikumbukireni ine, Inu Mulungu.” Akudalitseni, bwana. Mulungu akudalitseni,

dona. “Ndikumbukireni, Inu Mulungu.” Mulungu akudalitseni inu apa, mnyamata, Mulungu akudalitseni uko, dona. Kumbuyoko, msungwana, uko. Ndi inu kumbuyoko, dona. “Mundichitire ine chifundo, O Mulungu, pamene ndikuwona cholembedwa chiri pa khoma. Ndiri ndi nzeru zokwanira, nditi, kuwona kuti zimene zanenedwa kuchokera mu Baibulo, usiku uno, kuti kumeneku ndi kubwereza kwa mbiriyakale.”

<sup>102</sup> Tiri pamapeto. Palibe chimene chingathandize. Chinthu chimene chidzawononge dziko chiri mmanja a amunthu wochimwa

<sup>103</sup> Pangotsala enanso ochepa. Inu mukhoza kukhala wotsiriza amene anakonzedweratu kuti adze kwa Khristu. Pamene otsiriza adza, chiweruzo chidzafika; pangosowa chinthu chimodzi tsopano, chimenecho chikhoza kukhala inuyo. Kodi mungamulandire Iye usiku uno pamene tikuyembekezera?

<sup>104</sup> Manja ena 20 kapena 30 akwezedwa. Tsopano tiribe malo pano kuti tiyitanirepo anthu ku guwa, kuti anthu abwere kutsogolo kuno, chifukwa palibe malo ena alionse. Koma ine ndikufunsani, ndithudi, kuti mukhale owona mtima ndi kumvera ku liwu la chenjezo. Khalani owona mtima ndi kufunsa Khristu, pa malo pomwe mwakhalapo, “Ambuye, ndichitireni chifundo ine, wochimwa, ndi kundilandira ine pamene ndikupyola kupita kutseri kwa chopimba cha chifundo. Ndisanachimwe kupyola masiku anga a chisomo, ndichitireni chifundo ine, Ambuye,” ndipo Iye akuchitirani.

Tsono pempherani chotero pamene ndizikupempherani.

<sup>105</sup> Ambuye odala, ife tayima pano pa chikhalidwe chovuta usiku uno. Pamene tikuwerenga Mawu Anu, ndi kudziwa kuti pafupifupi ora lina mawailesi akhoza kugundika, ndipo magulu a gwedemula nafika poyimba. “*Mfupi, Mulungu Wanga, Ndi Inu,*” koma zidzakhala zochedwa pamenepo, chiweruzo chitafika. Mamisayelo alozetsedwa kwa ife. Chiwonongeko, mitunda ndi mitunda, zolemera ndi zolemera za—zosesa dziko lapansi za mphamvu za atomiki, ndi zina zotero, zimene zidzayatse dziko lonse lapansi ndi moto. Ndipo ziri m’manja a munthu wodzazidwa ndi machimo. Ndipo Baibulo limati kuti uno ndi momwe zidzachitikire. Ndipo ife tikuwona cholembedwa pa khoma.

<sup>106</sup> O, Ambuye Mulungu, ine ndiwosakwanira kuti ndiyese kubweretsa Uthenga monga uwu kwa anthu awa. Ndipo ndikungodziwona momwe ndiriri wamng’ono, kuyima pano, kuyesa kupereka phunziro ili, koma Inu mundikhululukire ine chifukwa cha mbali imene ndikulephera kuyichita. Komabe, kuchokera mu mtima wanga, ine ndikukupemphani Inu kuti mumize Uthenga umenewu, mwa njira imene Inu mukanachitira, m’mitima yawo, pakuti ndikuwona nthawi ikuyandikira. Ndipo ndichitireni chifundo, Mulungu, ndi



kupulumutsa aliyense, ndi kuwadzaza ndi Mzimu Woyera. Ndipo mulole iwo akhale ana Anu, okutidwa Mwauzimu ndi ubwino Wanu, ndi kulandira chitetezo kuchokera kwa Ambuye Yesu.

<sup>107</sup> Pakuti, fuko lathu siliri lotetezeka. Timangoganiza kuti tiri. Chimodzimidzinso anthu a Ufumu wa Babeloni ankaganiza chotero, koma, nthawi yonseyo, panali fuko loyipa mtima likugwira ntchito. Ndipo pakhala pali fuko loyipa likugwira ntchito, mpaka tsopano tikudziwa kuti iwo ali patsogolo pathu, ndipo ife tiri kwa chifundo chawo.

<sup>108</sup> Ambuye, Mpingo uli kwa chifundo Chanu. Iwo adzawononga; komabe Inu mudzatenga Mpingo Wanu. O Ambuye, titengeni m'manja a chisamaliro Chanu, usiku uno. Ndipo tidalitseni ife chifukwa cha Yesu; ndipo mu Dzina Lake ife tikupempha. Amen.

<sup>109</sup> Mosafuula, mwa kamphindi. Khalani modzichepetsa.

Mofatsa ndi mokoma Yesu akuyitana  
Kuyitana inu ndi . . .

Pamene tikuyimba tsopano, lingalirani.

Pa khomo Iye akudikira ndi kuyang'anira,  
Kuyang'anira inu ndi ine

Idzani Kunyumba (kuti? Kwera kuno, Kwera  
m'mwamba.)

Inu olema idzani Kunyumba  
Moona mtima, mokoma Yesu akuyitana,  
Kuyitana ochimwa, idza Kunyumba!

[M'bale Branham ayamba kung'ung'uza *Mofatsa ndi Mokoma—Mkonzi*].

<sup>110</sup> O, kodi siyingakhale nthawi yodabwitsa kuti zimenezo zichitike tsopano! O, zonse ziri bwino, nthawi iliyonse Iye ndi wokonzeka. Amen! Ndiri wosangalala pa kumudziwa Iye. Ndiri wosangalala kuti thupi lotopa lokalambali, limene likukwinyata pamwambali, lidzasinthika mwa kamphindi, mwa kuthwanima kwa diso. Ine ndidzabwerera ku unyamatanso, kukhala moyo mwa nthawi zosatha.

Okalamba adzakhala anyamata nthawi zonse  
Osinthidwa mwa kamphindi ka nthawi;  
Osafa, kudzakhala ofanana ndi Iye  
Nyenyenzi ndi dzuwa adzaziposa kuwala.

Ndi mwayi wotani uwo! Musamukane Iye.

O, momwe mudzafunira Iye kuti anene,  
"Wachita bwino,"

Pa Tsiku la Muyayalo!

Musamukane Mpulumutsi wokondedwa mu  
mtima wanu,

Musamukane Iye konse. (Lolani kuti ukhale  
usiku uno.)

<sup>111</sup> Ndi angati amene mukumukonda Iye ndi moyo wanu wonse, ndipo muli okonzeka ngati Iye angadze? O, ndife othokoza bwanji! Kodi simukumva ngati mwachita kuwotchedwa tsopano, mkatimo? Uthenga, ife tikutsukidwa ndi madzi a Mawu. Tangofikirani pafupi ndi inu, ndi kugwirana manja ndi wina, ndi kuti, “Mulungu akudalitseni. Ndikungomva bwino kwenikweni. Mulungu akudalitseni, wapaulendo. Mulungu akudalitseni, mlongo, m’bale.” Ndife amwenda-mnjira tiri paulendo.

Kuyenda pa njira yopambana yakale,  
 Kuwuza anthu konse ndipita,  
 Kuli bwino ndikhale M’khristu wachikale,  
 Ambuye,  
 Koposa chirichonse ndichidziwa.

<sup>112</sup> Tsopano tikadali mu mphindi iyi ya kulemekeza, ndikukhulupira kuti nthawi yatha kwakuti tingayitanire mzere wa mapemphero. Tiyeni...Ndikukhulupira Mzimu Woyera ali wokondwa nalo, gulu lalikulu limene ladza kwa Khristu. Tsopano mukadzipezere mpingo mofulumira, batidzidwani ndi kumapita ku mpingo umenewo, mpingo wabwino wodzazidwa ndi Mzimu, ndipo kumeneko khalani mwa moyo wanu wonse.

<sup>113</sup> Ndi ntchito zANJI zimene Khristu analonjeza kuti adzachita? Iye anati, “Ntchito zimene ine ndizichita, inunso mudzazichita.” Ndiyeno Kukhalapo Kwake kuli pano. Ndipo, ine ndikudziwa, anzanga. Ine—Ine ndikudziwa, mopanda mthunzi wa chikayiko, kuti Yesu ali pano. Pali Mwamuna pano, ndi Mwamuna yemwe uja anayenda ku Galileya. Ndi Mwamuna yemwe uja amene anatiwombola ife ndi Mwazi Wake, nakuchiritsani inu ndi mikwingwirima Yake. Ndipo Iye ali pano kudzawonetsa ndi kudzachita chirichonse chimene Iye anachichita, pakuti Iye ndi Ambuye Yesu yemwe uja.

<sup>114</sup> Tsopano tiyeni tipemphere kwa kamphindi chabe, mwakachetchete. Ingokhalani mwapemphero pamene ndikuyesa kupeza lingaliro la Mzimu Woyera.

[M’bale Branham adikira kaye—Mkonzi].

<sup>115</sup> Koteru, nyimbo yokongolayo, momwe anthu ali mu chisautso usiku uno akanakonda kuyimva imeneyo! Anthu amene anakhala poyamba m’ mipando yomwe mwakhalapo usiku unoyi, anamva Uthenga, ndipo tsopano anamwalira, ali mu chisautso usiku uno; momwe iwo akanafunira kukhala pamene mulipo; koma anapita kale tsopano. [M’bale Branham adikira—Mkonzi].

<sup>116</sup> Ambuye, Inu Amene munapanga Kumwamba ndi dziko lapansi, Inu Amene munatumiza Ambuye Yesu odala ku dziko lapansi; ndipo mwa Iye munali chidzalo chonse cha Mzimu. Ndipo Inu munati, kupyolera pa milomo Yake, “Ine ndi Mpesa, inu ndi nthambi. Mpesa siumabereka zipatso pa Wokha, koma nthambi zimabereka zipatso.” Ndikupemphera, Mulungu, kuti

mudziwonetsere Nokha usiku uno, pakati pathu, kuti anthu awa akhoze kudziwa kuti Uthenga umene walalikidwawu, umene wachokera kwa Inu, kuti Inuyo mukutichenjeza ife kuti tikonzeke, ndipo masiku otsiriza afika.

<sup>117</sup> Pali anthu ambiri odwala amene akhala apa, Ambuye. Apatseni chirimbitso, kuti akhoze kuchiritsidwa, pakuti tikufunsira izi kuti zipereke ulemerero kwa Mulungu. Tsono, Ambuye, pamene tikudzipereka tokha kwa Inu, monga Mpingo wa Mulungu wamoyo; powona, ndikuganiza, dzanja lirilonse pano linakwezedwa. Ndipo ine ndikufunsani Inu, usiku uno, Ambuye, kuti mutichitire china chapadera. Ndipo ingoperekani tsopano kuti anthu awa akhale odzipereka okha mwakuti Mzimu Woyera ungayende kupyolera mwa iwo, ndi chikhulupiriro chotero, ndi kuti ine ndikhoze kudzipereka ndekha kwa Inu ndipo Inu mukhoze kugwira ntchito kupyolera mu mphatso Zanu ndi kudzitsimikizira Nokha pakati pathu kuti, pakhoza kukhala alendo pakati pathu. Izi tikupempha mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>118</sup> [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]...pakuti Iye nthawi zonse amawonetsa chifundo chiweruzo chisanadze. Ine ndingofunsa alaliki kuti atsale pomwepo, napemphera. Tiyeni tipemphere.

<sup>119</sup> Ndipono, kwenikweni, ndakhala ndikulalikira, ndipo ine—ndingofunsa mwina anthu amene ali kutsogolo kuno, kaya kwina kulikonse komwe muli, ingoyambani kunena izi. Baibulo limati kuti, “Iye ndi Wansembe amene akhoza kukhudzidwa ndi zowawa zathu.” Chabwino, ndiye, ngati Iye ali Wansembe Wamkulu amene anali dzulo, Iye ali chimodzimodzi lero; ndiye zochita zake zimene Iye anazichita dzulo, azichita lero ngati Iye alidi chimodzimodzi. Sichoncho? Kotero ngati Iye angakhudzidwe tsopano, inu mumukhuze Iye ndi zowawa zanu, ndipo muloleni Iye alankhulenso ndi inu.

<sup>120</sup> Tangoganizani, pamene Iye anayima pakati pa chigulu cha anthu monga ichi tsiku lina, panali mwamuna amene anadza wotchedwa Petro, kani dzina lake linali Simoni. Ndipo Iye anati, “Dzina lako ndi Simoni. Ndiwe mwana wa Yonasi. Koma, kuyambira tsopano, udzatchedwa Petro.” Nanga iyeno anadzasandulika wotani? Mtumwi wokondedwa.

<sup>121</sup> Pamene Filipino anampeza Natanieli, ndipo iye atabwera, Ambuye anati, “Onani M’Israeli amene mwa iye mulibe chinyengo,” mwa mawu ena, “Mkhristu, munthu woona mtima.

Anati, “Mwandidziwa bwanji, Rabbi?”

<sup>122</sup> Anati, “Filipo asanakuyitane iwe, pamene unali pansu pa mtengo, ndinakuwona iwe.”

<sup>123</sup> Mkazi amene anali ndi vuto la magari anabwera. Ambuye anayang’ana pakati pa anthu.

<sup>124</sup> Iwo anali kuganiza kuti ntchito Zake zinali za M'dierekezi, ndipo anati mu mtima mwawo, "Ameneyu ndi Belezebule." Ndipo Iye anadziwa zolingalira zawo. Sichoncho?

<sup>125</sup> Iye anati, "Ine sindimachita kanthu mpaka Atate atandiwonetsera poyamba. Ndipo ntchito zimene Ine ndikuchitazi, inunso mudzazichita." Kotero Iye ayenera kutero, ngati Iye akugwira ntchito mu Mpingo Wake, chifukwa amenewo ndi Mawu Ake.

<sup>126</sup> Tsopano ine ndikufuna kukufunsani inu. Ngati mu gulu ngakhale anthu awiri kapena atatu, Ambuye akawalola kuti akhale ndi chikhulupiriro chokwanira kugwira chovala Chake, ndipo lye awberera mwa Mzimu Woyera nadzachita chimodzimidzi momwe Iye anali kuchitira pamene anali pa dziko lapansi, kodi mungakhutitsidwe ndi kumulandira Iye ngati Mchiritsi wanu? Mungatero? Nenani, "Amen," ngati mungatero. [Mpingo uti, "Amen."—Mkonzi] Ambuye akupatseni, ndiro pemphero langa. Tsopano zingopempherani. Ndipo ngati inu. . .

<sup>127</sup> Ndi anthu odwala angati pano amene akufuna kuchiritsidwa, kwezani manja anu. Kulikonse, chabwino, anthu odwala amene mukufuna kuchira.

<sup>128</sup> Tsopano, ngati pali wina aliyense mu nyumba ino amene ine. . . Ine sindikudziwa aliyense amene ndikumuyang'ana apa.

<sup>129</sup> Ndikuganiza uyu ndi Rosella wakhala apayu, mtsikana wamng'ono amene anali chidakhwa, amene anayitanidwa mu msonkhano kwina kwake, anali chidakhwa, ndipo madokotala anali atamulephera. Iyeyu, pamene Ambuye anamuyitana, mtsikanayu akudziwa kuti ine ndinali ndisanamuone ndi kale lomwe kapena kumudziwa konse. Ndipo Ambuye anamuwuzza zonse za moyo wake ndi momwe analiri, namuwuzza kuti akhala bwino. Ndipo ndi uyu pano usiku uno, chikho cha chigonjetso cha chisomo cha Mulungu. Chidakhwa, mpaka kuti madokotala molandirizana anamulephera, ngakhale Othandiza Zidakhwa. Ine ndikumudziwa iyeyu.

<sup>130</sup> Koma, mwina, ndikutsimikiza kuti m'bale uyu akundiyan'ana ineyu, amene wakhala apa atavala suti ya mbuu, ndi m'bale amene amatibweretsera maluwa. Ndikukhulupirira kuti ndi choncho. Ine—sindingathe kuganizira dzina lake tsopano. Iye anafika kunyumba kwanga posachedwapa, ndi M'bale Boze; Shultz, M'bale Shultz.

<sup>131</sup> Kupatula amenewa, ndikuganiza kuti ndinawawona M'bale Fred Sothmann pa timphindi pang'ono tapitato, pena pake mu nyumba ino, koma ndayiwalala kuti panali pati tsopano. Komabe, iwo anali, ali mom'muno pena pake.

<sup>132</sup> Ndipo ine—sindikudziwa wina aliyense. Koma Mulungu akukudziwani inu nonse. Ngati musingopemphera ndi kufunsa Mulungu, yesani chikhulupiro chanu.

133 Ndipo wina wa inu asayendeyendenso tsopano. Khalani mogonjera kwa mphindi zochepa zikudzazi. Tsopano, “*Kungokhulupira.*” ngati mutatero. Ndipo mongogonjera monga momwe mungathere kwa mphindi zochepa, ndipo ingokhalani mwa chete. [Wa limba ayamba kuyimba *Kungokhulupira*—Mkonzi].

134 Tangoganizani, Khristu anachita kulonjeza. “Kanthawi, ndipo dziko silidzandiwonanso Ine; koma inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine, . . . Ine, osati wina.” *Ine* ndi pulonauni wa umwini. “Ine ndidzakhala ndi inu mpaka ku chitsiriziro cha dziko. Zinthu zimene Ine ndikuchita, mudzazichitanso inuyo.” “Yesu ali yemweyo dzulo, lero ndi nthawi zonse.” Sichoncho? Ziyenera kukhala zoono!

135 Chabwino, ndiri woyamika kwambiri kwa Ambuye. Ndikungofuna . . . Mukhoza kutukula mitu yanu ngati mukufuna kutero.

136 Pompano pakonapa, pali dona amene wakhala pakonapa. Ndi mkazi wa chikaladi. Dona, ine sindikukudziwani inu. Mulungu amakudziwani inu. Koma pali Kuwala uko pamwamba pa mkaziyo tsopano. Iye ali ndi . . . Ngati Ambuye atandiwululira ine vuto lanu, ndi chimene mukupempherera, kodi mukhulupirira kuti ndi Ambuye Yesu amene akukuthandizani? Inu muyenera kukhala kuti muli m’avuto, kapena chinachake chimene mukufuna, chifukwa icho chiri pamenepo.

137 Onani, anzanga, inu mukuti, “Nanga ine ndisakuchiwona.” Zimenezo ndi zotheke kuti inu simungathe kuchiwona Icho. Ine ndikuyang’ana molunjika pa Icho. Mwaona? Inu muti, “Chabwino, M’bale Branham, ngati inu mungachiwone ndi mphamvu ya m’thupi lanu, ine ndikhozanso.” O, ayi.

138 Paulo anachiwona Icho, Yesu uyu mwa mawonekedwe a Kuwala, ndipo iwo amene anali ndi iye sanachiwone Ichi. Mwaona? Amagi anawona Nyenyezi, Kuwala kumene kunawatsogolera iwo, koma palibe winanso amene anakuwona Iko. Ndi za kwa ena okha. Ndi mphatso.

139 Mkaziyo ali ndi vuto la misempha. Ndi choncho. Inu mulinsu ndi vuto la mtima. Ndi momwemo ndithu. [Mkaziyo ati “Ulemerero! Aleluya! Zikomo kwa Inu, a Yesu! Aleluya!”—Mkonzi.] Mverani. Dzina lanu ndi, amakutchani Essie. [“Ndi momwemo.] E-he. Dzina lanu lotsiriza ndi Upshire [Ndi momwemo, M’bale Branham”] Inu mumakhala kumpoto kwa Msewu wa Cleveland. Adiresi yanu ndi 1264, Izo ndi zoono chimodzimodzi. [Kumeneko ndiye komwe ine ndimakhala.”] Mwa . . . Inu munakhuza Chinachake, dona. Inu mukudziwa kuti simunandigwire ine.

140 Msungwana uyo amene wakhala pafupi ndi inu pamenepo, iyenso akupemphera. Ndipo iye akupempherera wina wake, ndipo ameneyo ndi, amayi wanu, ndipo ali ndi vuto la china

chimene chalakwika mu mapapo awo. Ndipo inu muli ndi chilumikizo chinachake ndi amayi awa *kuno*, inu ndi mpongozi wao wamkazi. Ndipo dzina lanu ndinu Magireti. Ndi choncho. Ndipo inu mumakhala ku malo amodzi. Ndikukuwonani mukutuluka, ndi kulowa.

<sup>141</sup> Mukuganiza chiani za zimenezi, bwana, inu amene mwakhala pafupi nawonu? Kodi mukukhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu? Mukutero? Ngati Ambuye atandiwululira ine vuto lanu kuti ndi chiyani, kodi mumulandira Iye? Inu muli ndi vuto la m'mimba. Ndi chomwecho. Ngati ziri choncho imani pa mapazi anu. Momwemo. Inu ndi mlaliki.

Ndithudi, inu mukuti, “Waona zovala zake za ubusazo.”

<sup>142</sup> Chabwino, pambali pa zimenezo, wina akhoza kuganiza kuti ndinu a Presbyteria, koma inu ndi mlaliki wa Chipentekosite. Ndi zoon. Amen. Manjenje anu ndi amene anayambitsa zirona za m'mimba. Zathano. Pitani kunyumba ndi kukakhala bwino, m'bale. Amen.

Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu! Musakayikire konse.

<sup>143</sup> Mukuganiza chiyani, amene mwakhala apa? Inde. Kodi mukukhulupira? Mukukhulupira kuti ine ndi wantchito wa Mulungu? Kapena, mukufuna china chochokera kwa Mulungu? Ngati Mulungu atandiululira ine chimene mukufuna, kodi mukhulupirirano kuti ndi Zauzimu zikuchitika? Kodi mukukhulupirira kuti ndi chimodzimodzi zimene Yesu akananena? Ndi mtima wanu wonse? Inu muli ndi chotupa, ndipo chotupa chimenecho chiri m'chiuno mwanu. Ndi momwemo. Ndipo inunso muli ndi vuto la m'mimba, layambitsidwa chifukwa cha manjenje anu. Ndi choncho. Dzina lanu ndi Eva May. Readman ndi dzina lanu lotsirizira. Inu mumakhala ku msewu, 1378 West 13th Street. Izo ndi zolondola. Kuti mudziwe kuti ndine wantchito wa Mulungu, uyo ndi mwana wanu wamkazi amene wakhala pamenepoyo. Mukumufunira pemphero iyeyo. Mwana wamkaziyo ali ndi vuto lotaya magazi, ndipo limadza pa iye pamene ayamba kukhala wotekeseka kapena kuyamba kulira kwambiri ndithu. Zimenezo ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Kam'nyamata kali pa menepoko ndi m'chimwemwe wake. Ndi choncho. Kam'nyamata kamenekonso, mukukafunira pemphero. Iyeyo akuvutika ndi kusachita chimbudzi, ndipo kulemera kwa thupi lake kwatsika kwambiri posachedwapa. Sanatero? Zimenezo ndi PAKUTI ATERO AMBUYE.

<sup>144</sup> Mkazi wachizungu amene wakhala pafupi ndi inuyo, akukhala ngati akusautsika ndi chinachake. Kodi mukukhulupirira, mlongo? Mukukhulupirira kuti Mulungu watumiza Mwana Wake, Yesu Khristu, kudzawonetsera kwa m'badwo wa amitundu kuti Iye akudza posachedwapa? [Mlongo

ati, “Inde, bwana”—Mkonzi.] Inu muli ndi vuto la amwanabele amene mukuvutika nawo, ndiponso vuto la kathumbo, ndipo muli ndi manjenje. Inu si a mu mzinda uno konse. Inu ndi ochokera ku Detroit. Nambala yanu, kumene mumakhala, ndi 12134 Fandler Street. Ndi momwemo. Detroit, Michigan. Inu ndi M’taliana. Dzina lanu ndi Viola P.o.l.o.f . . Polofmba. Aha. Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu, ndipo landirani zimene mukupempha.

145 Mukuganiza chiyani, pansi ku mbali *iyi*? Kodi mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse?

146 Nanga bwanji inu, adona amene mwakhala aponu? Kodi mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, dona wamng’ono pamapetopo? Chabwino, aliyense wa inu, ziribe kanthu. Mukuganiza chiani, inu pamenepo pafupi ndi Iye? Kodi mukukhulupirira ndi mtima wonse, amayi aang’ono inu, amene mwakhala ndi kumandiyang’ana? Mukuganiza chiani za zimenezi? Mukukhulupirira kuti Ambuye Yesu akhoza kukuchizani misempha yoberekerana imene ikukupwetekaniyo? Mukutero? Mwina mukhoza kuganiza motere, kuti mungakhulupirire kwambiri ngati nditakuuzani kuti amuna anu ali ndi vuto la khutu. Inu mumafuna kuti iwo apemphereredwe. Ndi momwemo ndithu. Kodi mukundikhulupirira tsopano? Simumamvetsa poyamba. Izi zakhala ngati zakudzutsani kuti muchite chinachake, chifukwa pomwepo munalandira machiritso anuno.

147 Inu munakweza dzanja lanu, pafupi ndi iye, dona. Mukuganiza chiyani za zimenezi? Mukukhulupirira kuti Mulungu akuchiritsani? [Mkaziyo ati, “Ndikudziwa kuti Iye atero.”—Mkonzi.] Mukuvomereza? Chabwino, ndiye vuto lanu la nyamakazi likusiyani.

148 Munaganiza chiani, bwana? Inu amene munagwedeza manja anu. Mukukhulupirira kuti Mulungu achiza vuto lanu la mtima, nakukhalitsani bwino? Kodi mukukhulupirira kuti Iye akhoza?

149 Inu amene mwakhala, kumamuyang’ana iye pamenepo, kodi inu mukukhulupiriranso? Inu mukufuna Mulungu. . . Inu munali ndi vuto la mtimanso, sichoncho? Inde. Ndiponso munali ndi vuto la kuthamanga kwa magazi. Ndi choncho. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani? Ndiye mukhoza kuwalandira iwo.

Kodi simukukhulupirira? Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu!


150 Bwanji pansi *apa*? Inu, bwana, amene mwakhala pa mapeto a mpando, mukukhulupirira? Muyenera, mwangochiritsidwa kumene. Mwaona? Munali ndi vuto la phazi, sichoncho? Mukukhulupira kuti Ambuye Yesu. . . Koma mukupempherera wina wake tsopano, ameneyo ndi m’bale wanu. Ndipo iye ali ku Wisconsin. Angomuchita opareshoni ya mapapo kumene,

theka lake lachotsedwa. Ndi choncho. Mukukhulupirira? Ndiye mukhoza kulandira chimene mwapempha. O, lidalitsidwe Dzina la Ambuye!

Ndidzam'yamika, ndidzam'yamika  
 Yamika Mwanawankhosa wophedwera  
 ochimwa;  
 Mpatseni Iye ulemerero inu anthu onse,  
 Poti Mwazi Wake watitsukira banga lirilonse.

<sup>151</sup> Ambuye Odala, tidzakuonani Inu tsiku lina mukudza M'mwamba. Ife tikudziwa Inu muli pano mu Thupi lauzimu, mwadzizindikiritsa Nokha kwa ife mwangwiro. Dziko silingawerenge zimenezo, Ambuye. Ife sitikuyembekezera kuti atero, chifukwa Inu munati, "Iwo sadzandiwonanso Ine." Koma ife tikudziwa kuti muli ndi ana amene angakuoneni Inu. Tiri ndi ana amene akukudziwani Inu. Ndipo tiri othokoza chifukwa cha zimenezo.

<sup>152</sup> Ndipo tikupemphera tsopano kuti Inu muyendeyende m'nyumba muno, ndi Mzimu Woyera woposayo, ndi kuchiza munthu wodwala aliyense muno. Tsopano ingodzitengerani ulemelero Nokha, Ambuye. Anthuwa asangokhala mwakufa, koma akhoze kudzuka nawale, ndi kumpatsa Mulungu mayamiko ndi ulemelero. M'dzina la Yesu.

<sup>153</sup> Ngati inu mukumukhulupirira Iye, imani pamapazi anu ndi kumuyamika Iye ndi mtima wanu wonse. Ndi kusangalala mwa Ambuye Yesu, pakuti tsopano Iye akuchiza aliyense wa inu, mwa ulemelero Wake wopambana Waumulungu. Ambuye akudalitseni. Amen. 



*CHOLEMBEDWA PA KHOMA* CHA58-0108  
(The Handwriting On The Wall)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lachitatu madzulo, pa 8 Januwale, 1958, ku Lane Tech High School, mu Chicago Illinois, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©1991 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)